BAPTIST PUBLISHING HOUSE OF ZAMBIA
P. O. BOX 1995
LUSAKA, ZAMBIA

# Colinga ca Mulungu kwa anthu ace

charles Bellenger

AT14
NyA

# Colinga ca Muiungu kwa anthu ace

charles Bellenger

*GOD'S PLAN FOR HIS PEOPLE*
by Dr. Charles Bellenger
(Nyanja)
First Published in Zambia
October 1, 1973 by
The Baptist Publishing House of
the Baptist Mission of Zambia
P. O. Box 1995
LUSAKA, ZAMBIA

MAFUNSO

1. Kodi Yohane analalikira ciani?

2. Kodi Yohane anayesa kukondweletsa anthu?

3. Ndicifukwa ninji munthu ayenera kubatizidwa?

ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Luka 1:26-35 |
| Laciwiri | Luka 1:46-55 |
| Lacitatu | Luka 2:1-7 |
| Lacinai | Luka 2:8-20 |
| Lacisanu | Mateyu 2:1-12 |
| Loweruka | Yohane 1:1-12 |
| Lasabata | Yohane 1:15-28 |

ku Yudeya kuzamvera Yohane. Anafunitsitsa kumvera mau a Mulungu. Anamvetsera kwa Yohane, ndipo anakhulupilira uthenga wace. Ambiri anafunsa kuti abatizidwe. Yohane anabatiza iwo amene anatembenuka ndi ufunsa cikhulululukiro ca macimo awo.

Kodi Yohane anawauza ciani aja opembedza atsogoleri aci Yuda? (Ndime 7 ndi 10) Atsogoleri opembedza aja anacita phwete ubatizo wa Yohane. Anafuna kubatizidwa pamene iwo sanatembenuke muniira zoipa zawo zija. Yohane anawauza kuti anayenera iwo ku onetsa mitima yawo kuti anatembenuka.

Atsogoleri aja anayesa kuti iwo anali otembenuka cifukwa cakuti anali makolo a Abrahamu. Makolo athu sangatikhalitse ife bwino ndi Mulungu. Tiyenera kutembenuka ndiku khulupilira mwa Yesu kristu mwa ife tokha. Iyi ndivo njira cabe imene idzakhala bwino ndi Mulungu.

## YOHANE ANENA ZA YESU

Kodi Yohane anati bwanji paza Yesu? (Ndime 11 ndi 12) Ubatizo wa Yohane unali m'madzi. Ubatizo uyu sunkanasintha anthu kapena kucotsa anthu macimo awo. Cinali cifanizo cakuti kusintha kunadza m'mitima yawo. Yesu ankanadza kuzabatiza ndi Mzimu Woyera. Ici ci cikanabweletsa kusintha kwa m'katimwa mtima. Iyi ndiyo njira cabe imene anthu anaka khala osinthidwa.

Yesu anafunsa anthu kuti amukhululupilire iye. Anasonkhanitsa anthu monga mulimi amasonkhanitsa zolima zace m'munda. Iwo amene akhulupilira ndiwo ochedwa cimanga cabwino. Iwo amene sanakhulupilira angakhale oponyedwa ndi kulangika.

Yohane anali olangiza wa Mulungu. Anakonzera anthu njira yakuti angalandile Yesu ndikulandiranso ufumu wa Mulungu. Inunso mungakhale olangiza a Mulungu.



MAU OYAMBA

Mitu khumi ndi itatu mu miyezi inai iyi, tizakhala tikuona ku ombola kwa Mulungu ndi cifunilo cace ndi m'mene anasewenzela ndi anthu aci Hebri. Monga Akristu tiyenela kuphunzira m'mene tingacite muciombolo ca Mulungu ndi pangano. Ndipo tiyenera kuona m'mene tilili ife, ndi ku ona m'mene tingathe kucita cifuno ca Mulungu masiku ano.

Mau athu a Mulungu muphunziro limeneli azacokela maka maka mucipangano cakale.

Colinga ca phunziro ili ndi ku kuthandizani kumvera m'mene Mulungu a masewenzela ndi athu kapena ndi mtundu wa padziko lino ndi m'mene atanthauzila cifunilo cace. Ndikuti mungathe kuona ndi kudziwa malo anu mwa Mulungu ndi m'mene acita cifuno. Bwanji nanga osazipeleka inu nokha kwa Mulungu? Welengani Yohane 17:18.

*loyandikana ndi Yordano; 6 nabatizidwa ndi iye*
*mu mtsinjewo wa Yordano. alikuulula macimo ao.*
*7 Ndipo iye pakuona ambiri Afarisi ndi a Asaduki*
*akudza ku ubatizo wace, anati kwa iwo, Obadwa*
*a njoka inu, ndani anakulangizani kuthawa*
*mkwiyo ulinkudza? 8 Onetsani inu zipatso zaku-*
*yenera kutembenuka mtima: 9 ndipo musamayesa*
*kunena mwa inu nokha, Atate wathu tiri naye*
*Abrahamu; pakuti ndinena kwa inu kuti mwa miya-*
*la iyi Mulungu akhoza kuukitsira Abrahamu ana.*
*10 Ndiponso tsopano lino nkhwangwa yaikidwa*
*pa mizu ya mitengo: cifukwa cace mtengo uli*
*wonse wosabala zipatso zabwino udulidwa nupo-*
*nyedwa pamoto. 11 Inetu ndikubatizani inu ndi*
*madzi kuloza ku kutembenuka mtima: koma Iye*
*wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu,*
*amene sindiyenera kunyamula nsapato zace; Iyeyu*
*adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto:*
*12 couluzira cace ciri midzanja lace, ndipo*
*adzayeretsa padwale pace; ndipo adzasonkhanitsa*
*tirigu wace m'ciruli koma mankhusu adzatentha*
*ndi moto wosazima.*

Yohane anali munthu amene nthawi yaikuru anakhala kunja. Ndipo iye anabvala ca ubweya, ndipo anadya cakudya cimene anacipeza iye. Anakhala ndi moyo wapafupi.

Ndime ya ciwiri ndi yacitatu. zimatifotokozera ife zimene Yohane analalikira. Yohane anafunsa anthu kutembenuka. Kutembenuka kutanthauza ku coka ku macimo, ndi kusiya kumvera Satana. Citanthauza kuti, kutsata Mulungu ndi kumvera iye.

Yohane anati, ufumu wa Mulungu ulikuyandikira tsopano m'dziko. Ici cingacitidwe ngati anthu atembenuka, ndi ku lola Ambuye Yesu kukhala m'mitima yawo. Yohane anati cipangano cakale cinanena za iye amene anka nalalikira za kubwera kwa Yesu. Anayesa kuti ndiye. (Werengani: Yesaya 40:3).

Kodi anthu ana muyankha motani Yohane? (Ndime 5 ndi 6). Anthu anabwera kucokera

## MULUNGU ALANGIZA

PHUNZIRO LALIKURU LA M'BUKU LOPATULIKA:
Maliki 3:1-4, Mateyu 3:1-12; 11:7-10.

MAU A MULUNGU A PHUNZIRO LALERO: Mateyu 3:1-12

MAU APAMTIMA: *"Mau a wopfuula mcipululu, konzani khwalala la Ambuye, lungamitsani njira zace."*
*Mateyu 3:3.*

Olangiza ndiye amene abwera ndi kunena cimene cibwera patsogolo. Yohane mbatizi anali wotsogolera wa Mulungu. Yohane mbatizi anali mlaliki. Anadza pamene Yesu sanadze kuzanena kuti Yesu akubwera kuza lalikira.

Muphunziro latha, tinaphunzira zakubadwa kwa Yesu. Yesu anati onetsa ife Mulungu. Anagwira nchito ya Mulungu. Yohane mbatizi anagwira nchito ya Mulungu ndi ife omwe tingathe ku gwira nchito ya Mulungu Tingakhale, olongeza a Mulungu. monga Yohane mbatizi anatilongoza.

Tiyeni tiwerenge za Yohane ndi kuona m'mene analalikira monga wolongoza wa Mulungu.

Mateyu 3:1-12

1 *Ndipo masiku aja anadza Yohane mbatizi*
*nalalikira mcipululu ca Yudeya, 2 nanena, Tembe-*
*nukani mtima; cifukwa Ufumu wa Kumwamba waya-*
*ndikira. 3 Pakuti uyu ndiye ananenayo Yesaya*
*m'neneri, kuti Mau a wopfuula mcipululu, Konza-*
*ni khwalala la Ambuye, Lungamitsani njira zace.*
*4 Ndipo Yohane yekhayo anali naco cobvala cace*
*ca ubweya wangamila, ndi lamba lacikopa m'cuuno*
*mwace; ndi cakudya cace cinali dzombe ndi uci*
*wa kuthengo. 5 Pamenepo panamturukira iye a ku*
*Yerusalemu, ndi Yudeya lonse ndi dziko lonse*



ZA MKATIMU


| MUTU | | TSAMBA |
|---|---|---|
| 1 | NDI CIFUKWA NINJI A ISRAYELI ANAGAWANIKANA. | 1 |
| 2 | AMBUYE MULUNGU KAPENA BAALA. | 4 |
| 3 | CIWERUZO CA MULUNGU KWA ISRAYELI. | 7 |
| 4 | KU UNJIKANA KWA ANTHU A MULUNGU. | 11 |
| 5 | CIWERUZO CA MULUNGU PA A YUDA. | 15 |
| 6 | CIKHULUPILIRO CA MULUNGA COSIIDWA. | 20 |
| 7 | PANGANO LA KU BWELELANSO. | 24 |
| 8 | COSIIDWA CA MULUNGU CIMANGIDWANSO. | 28 |
| 9 | LAMULO LA MULUNGU LITSIMIKIZIDWA. | 33 |
| 10 | PANGANO LA AMBUYE YESU. | 37 |
| 11 | PAKATI PA CIPANGANO CAKALE NDI CATSOPANO. | 42 |
| 12 | MULUNGU ALI NDI IFE. | 46 |
| 13 | MULUNGU A LANGIZA. | 50 |

Anthu ambiri amaganizira Yesu pa nthawi ya khirisimisi. Khirisimisi siyenera kukhala nthawi yokha ya ku ganizira zaku badwa kwa Yesu. Yesu anadza kuzakhulukukira kwa iwo amene anacimwira Mulungu m'mitima yawo. Nthawi zonse pamene tipepha Mulungu kuti atikhululukire macimo athu tiyenera kukumbukira Yesu, ku badwa kwace Tiyenera kuyamika kwa Mulungu cifukwa ca mphatso yace yaikuru imene inapatsidwa mdziko lino lapansi.

Kodi mumakondwera kulandira mphatso? Mulungu akupatsani mphatso yaikuru imene mukalibe kuilandila. Mulungu akupatsani yekha kupyolera mwa Yesu Kristu mwana wace, Mulungu a dzakhala ndi inu ngati mudzala ndira Yesu kuti alamulire moyo wanu.

Kodi mukondwera ku patsa mphatso? Mungampatse munthu mphatso yaikuru mudziko muno. Mungathe kumolongaza munthu m'mene angakhalire ndi Mulungu mu umoyo wace ndi m'mene anga landilire Yesu kukhala olamulira mtima wace.

MAFUNSO

1. Kodi Yesaya m'neneri anayakhula motani kunena kuti mpulumutsi adzabadwa?

2. Ndicifukwa ninji Yosefe anafuna ku kwatira Mariya kuti akhale mkazi wace?

3. Ndicifukwa ninji Mulungu anatumiza Yesu mdziko?

ZOWERLENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Yesaya 53:1-12 |
| Laciwiri | Yesaya 54:1-10 |
| Lacitatu | Yesaya 55:1-13 |
| Lacinai | Yesaya 58:1-14 |
| Lacisanu | Yesaya 61:1-11 |
| Laweruka | Yesaya 64:1-12 |
| Lasabata | Mateyo 1:18-25 |

ankanatemedwa ndi miyala, kulingana ndi lamulo la a Yuda.

Mulungu anakhazika bvutoli la Yosefe, pakuti timawerenga mu Mateyu 1:20 kuti Mulungu anatuma m'ngelo kuti akambe ndi Yosefe, ndikumuuza zoonadi. M'ngelo anauza Yosefe kuti sayenera kukhala ndi manthapa kukwatira Mariya. Ananena kuti Mariya azakhala ndi mwana cifukwa ca mzimu Woyera.

Werengani Mateyu 1:21, amene ali mau atnu apa mtima. Ndime iyi ndi mtima wa nkhani yabwino. Yosefe anauzidwa ndi m'ngelo uja kuti azamucha mwana dzina lace Yesu. Dzina lakuti "Cipulumutso cicokera kwa Ambuye Yesu!" Aliyense amene akhulupilira mwa Yesu kuti ali mpulumutsi adzapulumuka.

## PANGANO LA MULUNGU LINAKWANILITSIDWA

Ndime 22 ndi 23 mu Mateyu mutu woyamba zitifotokozera zaku bwera kwa Yesu ndi ku kwanilitsidwa kwa mau am'neneri. Mulungu anauza m'neneri Yesaya kuti auze anthu za kubwera kwa Yesu. Werengani Yesaya 7:14. Mulungu ana kwanilitsa lonjezo lace pakutumiza mpulumutsi mdziko.

Dzina lina la mwana wa Mulungu ndi Emanueli, kunena kuti, Mulungu ali ndi ife. Mulungu abwera kwa ife mu njira ya umunthu mwa Yesu Kristu. Ngati tifuna kudziwa za Mulungu, tiyenera kudziwa za Yesu. Yesu atilo ngoza ife kwa Mulungu.

## YESU WA BADWA

Yosefe anakhulupilira mau a m'ngelo, ndipo sanali wa manyazi ku kwatira Mariya. Anakumbukira lonjezo la Mulungu ku pyolera mwa Yesaya m'neneri. Munthawi ya Mariya ndi Yosefe unali mwambo kuti mwamuna ache maina a ana. Pamene Yesu anabadwa, Yosefe anacita monga m'ngelo anamuuzira kapena m'mene ana mulamulira kuti amuchedzina Yesu.





## NDICIFUKWA NINJI AISRAYELI ANAGAWANIKANA

PHINZILO LALIKULU LA M'BUKU LOPATULIKA: Imafumu 11:28-16.

MAU AMULUNGU APHUNZILO LALERO: Imafumu 12:12-20, 26-28.

MAU APAMTIMA: *"Cilungamo cikuza mtundu wa anthu; koma cimo licititsa pfuko manyazi.*
Miyambo 14:34.

Yerobiamu anali wa m'ng'ono pamene Solomo anali mfumu. Solomo anazindikila kuti Yerobiamu anali mtsogoleli. Anaika Yerobiamu pa zinchito za mbiri kucokela ku mtundu wa Yosefe. Mulungu anali ndi pangano kwa Yerobiamu ndipo anatumiza m'neneri, Ahiya, kuti auze Yerobiamu pangano lace. Pamene m'neneri anoona Yerobiamu, anacosa cofunda cace ndi ku cidula m'magawo khumi ndi a wiri. Ndipo anauza Yerobiamu kuti atenge magawo khumipansipaja. Mulungu anati Yerobiamu anakamuika ku khala mfumu ya mitundu khumi. Solomo anamva pangano la Mulungu, ndipo sana kondwe ndi izi ai. Anayesa kupha Yerobiamu. Yerobiamu anathawila ku Aaigipto ku samala moyo wace.

## MFUMU WATSOPANO

Kulemela kwa Solomo ndi zonse zimene anapata zinatha. Solomo anafa ndi mwana wace Rehabiamu, amene ana yembekeza ku khala mfumu. Anthu anayenda ku Sekemu ku patsa Korona mfumu yatsopano. Yerobiamu anabweranso kucokala ku Aaigipto Anthu anakhala wotopa ndipo sanakondwe munthawi ya Solomo. Anthu anakhala naco cakusakondwa. Solomo anakhala akulipilitsa anthu ndalama za mbiri mdziko lace ku pele kedwa ku ufumu wace. Anthu anadza kwa Yerobiamu nati; "Tiyeni tipite kwa Rehobiamu kuti acoseko msoko," ndipo Rehobiamu anamva zimene anthu anamfunsa iye. Anauza anthu kubweranso m'masiku atatu, ndipo angawapats

iwo yankholace. Rehobiamu anapita ku anthu akulu akulu kufunsa zimene anganthe ku uza anthu. Akulu akulu aja ana muuza kuti acite zimene ana funsa anthu ndi ku wapatsayankho la bwino.

Rehobeamu pambuyo pace anapita ku acinyamata amene anali ndi zaka monga iye. Anafunsa anyamata aja zimene angathe ku uza anthu. Ana muuza ku wapatsa mau owuma. Kuwauza kuti azakhala iye wowuma mtima kupambana atate wace.

Yankho imene Rehobiamu anapatsa anthu inali yobwelera m'mbuyo nthawi ya anthu aci Hebri.

## UFUMU WAGAWANIKA

Pamene anthu ana uzidwa ndi Rehobiamu kuti msoko uzakhala pa mwamba, ana kalipa ndithu. Anati, "Tiyeni tipite ku manyumba anthu. Tizapita munjila yathu ndipo Rehobiamu azapita mu njila yace." Mitundu khumi ya Israyeli inakhazika Yerobiamu kukhala mfumu yao. Mitundu iwiri yosalila inakhala ndi Rehobiamu natenga ndzina Yuda kukhala umfumu wao.

Rehobiamu anafuna kutenga mitundu khumi ija ya Israyeli. Rehobiamu anatuma Adoramu ku anthu aja. Adoramu anagwira nchito kwa Davide ndi Solomo. Anthu ana mkana iye ndipo anamupha. Ndipo Rehobiamu anatuma ankhondo ace kuti acite nao nkhondo a Israyeli. Anatuma asilikali awa kuti a wabweza anthu aja. Koma Mulungu anatuma m'neneli kwa Rehobiamu. M'neneli anati, Mulungu ananena kuti osacita nkhondo ndi abale ako. Pita ku nyumba. Ufumu uyu onse ndi wa Mulungu. Umfumu unagawanikana mu khumi limodzi ndipo, awiri a mutundu wa ci Yuda.

## CIMO LA YEROBIAMU

Poyamba timaphunzila kuti Yerobiamu azakhala mfumu ya mitindu khumi. Mau a Mulungu



*sanafuna kunyazitsa iye, noyesa m'mtima*
*kumleka iye m'tseri. 20 Koma pakusinkhasi-*
*nkha-sinkha iye zinthu izi, onani. m'ngelo wa*
*Ambuye anaonekera kwa iye mkulota, nanena,*
*Yosefe, mwana wa Davide, usaope kudzitengera*
*wekha Mariya mkazi wako; pakutiico colandi-*
*ridwa mwa iye ciri ca Mzimu woyera. 21 Ndipo*
*adzabala mwana wamwamuna, ndipo udamucha dzina*
*lace Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace*
*ku macimo ao. 22 Ndipo zonsezi zinakhala kuti*
*cikacitidwe conenedwa ndi Ambuye mwa mneneri,*
*ndi kuti, 23 Onani namwali adzaima, Nadzabala*
*Mwana wa mwamuna, Ndipo adzamucha dzina lace,*
*Emanueli; ndilo losandulika. Mulungu nafe.*

*24 Ndipo Yosefe anauka tulo tace. nacita*
*monga anamuuza m'ngelo wa Ambuye, nadzitenge-*
*ra yekha mkazi wace; 25 ndipo sanamdziwa iye*
*kufikira atabala mwana wace; namucha dzina*
*lace Yesu.*

Pafupi pamiyezi isanu ndi umodzi phunziro lathu linali la Abrahamu. Mulungu analonjeza kudalitsa Abrahamu. Pambuyo pace tinaphunzira za Davide. ndipo Mulungu anauza Davide kuti umfumu wace uzakhala cikhalire. Mulungu anati Yesu Kristu adzabwera kupyolera ku m'badwo wa Davide. Tinga mganizire Yesu, monga munthu kubwereranso kwa Adam. munthu woyamba. Werengani Luka 3:38. Maonekedwe a Yesu onse amapita kwa Mulungu. Werengani Yohane 1:1, 14.

Mu mau a Mulungu mu mutu woyamba wa Mateyu, timapeza kuti Mariya ndi Yosefe anali wopangana za kukwatirana. Inali nthawi iyi, pamene iwo asanakwatirane, Mariya anakhala ndi pathupi. Pakuphunzira zimeneizi, Yosefe anakwiya kwambiri. Mkazi wa ci Yuda anakhala wokhulupilika kwa mwamuna amene anafuna kukwatilana naye.

Kulekana nafunidwa kuti asiye pangano lawo, koma Yesefe sanafune kubvutitsa Mariya. Sanafune kuti asiyane mu nyumba ya mbwalo. Ngati Mariya anali ndi mulandu wa cigololo,

## MULUNGU ALI NDI IFE

PHUNZIRO LALIKUKU LOCOKERA M'BUKU LOPATULIKA:
Mateyu 1,

MAU A MULUNGU A PHUNZIRO LA LERO: Mateyu 1:1, 18-25

MAU APAMTIMA: *"Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo adzamucha dzina lace Yesu, pakuti iyeyo adzapulumutsa anthu ace ku macimo ao."*
*Mateyu 1:21.*

Masabata awiri apitao ma phunziro athu akhala akucokera mu buku la Yesaya. Tina phunzira kuti Mulungu analonjeza ku tumiza mpulumutsi. Pamene Mulungu anakhazika mfumu Davide wa Israyeli, Mulungu analonjeza kuti ufumu wace udzakhala wacikhalile Mulungu anasimikiza mau ace pakutumiza mwana wace, Yesu Kirstu. Make wa Yesu, m'namwali Mariya anali m'badwo wa mfumu Davide.

## MULUNGU ANADZA KUPYOLERA MWA YESU

Takhala tili kuphunzira m'mene Mulungu analonjezera anthu zakuza kwa mpulumusi mu cipangano cakale. Tsono tiyamba phunziro lathu mu cipangano catsopano. Iliphunziro ndi lakubwera kwa mpulumutsi, Yesu Kirstu. Timaona kuti zakubwera kwa Yesu. ndimo m'mene Yesaya ananenera m'mene cizakhalira.

Mateyu 1:1, 18-25

*1 Buku lakubadwa kwa Yesu Kristu mwana wa Davidi, mwana wa Abrahamu.*

*18 Ndipo kubadwa kwace kwa Yesu Kristu kunali kotere; Amai wace Mariya anapalidwa iye ali ndi pakati mwa Mzimu Woyera. 19 KOma Yosefe, mwamuna wace, anali wolungama, ndiponso*



akhala woona. Yerobiamu ana lephera Mulungu. Anakhala wa mantha. Anamva mantha kuganiza kuti anthu onse ace aja, azabwerelanso kwa Rehobiamu na umfumu wace. Mantha awa kapena kusapanda cikhulupiliro mwa mulungu, cina bweletsa yerobiamu ku cimwa. Mu buku la 1 Mafumu 12:28 tima welenga kuti Yerobiamu anapanga ana awiri a ng'ombe a golidi nanena ku anthu ace kuti a pembedze mafano aja. Chifukwa ca kusa khulupilira mwa Mulungu, Yerobiamu ana cimwila Mulungu.

## MAFUNSO

1. Ndicifukwa ninji ufumu wa Yerobiamu una onongeka?

2. Chifukwa ninji Yerobiamu ana cimwa? Cimo lace linali lotani?

3. Ndicifukwa ciani tiyenera kukhala ndi cikhulupiliro mwa Mulungu? (Welengani Ahebri 11:6).

## ZAKUWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | 1 Yohane 5:1-11 |
| Laciwiri | 1 Yohane 5:12-21 |
| Lacitatu | 1 Yeremiya 17:1-8 |
| Lacinai | Yeremiya 31:27-37 |
| Lacisanu | Yeremiya 33:1-26 |
| Loweluka | Marko 3:22-41 |
| Lasabata | Ezekieli 11:13-21 |

## MULUNGU AMBUYE KAPENA BAALA

PHUNZILO LALIKURU LA M'BUKU LOPATULIKA: 1 Mafumu 17-18.

MAU AMULUNGU APHUNZILO LA LERO: 1 Mafumu 18:20-40.

MAU APAMTIMA: *"Imvani, Israyeli, Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye umodzi. Ndipo muzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu onse, ndi moyo wanu wonse, ndi mphamvu yanu yonse.*
*Dauteronomo 6:4-5.*

Mphunzilo lathu lero tizaphunzila za Eliya, m'neneli, ndi mfumu Ahabu. Iwowa anakhala kumbali yakupoto mu dziko la Israyeli. Ahabu ana kwatila Yezebeli mkazi wocokela kudzikolina. Mkazi uyu ana pembeza Mulungu wochedwa Baala. Pamene anabwela mu Israyeli anadza ndi mafano ambiri ansembe. Yezebeli ana tsogolela Ahabu ku pembeza Baala. Anali ndi anthu a Mulungu amene ana phedwa. Pambuyo pace anthu a Baala a Israyeli ana yamba kupembeza.

### KULIBE MVULA

Tsiku lina Eliya, m'neneli, anati, "Mulungu ali wa moyo. Chifukwa Mulungu aliwa moyo, simuzaona mvula kapena mame. Simuza ona mvula mpaka ndi tanena conco." Ndipo Mu Mulungu ana tsogolela Eliya ku mbali ina ya mdziko muja. Anakhala kufupi ndi kamsinje. Mbalame zinamubwelesela ca kudya. Mvula siinagwe ai. Pambuyo pace kamsinje kaja sikanakhale ndi madzi. Mulungu ana tumanso Eliya ku dziko lina. Anauza Eliya kuti mkazi wa masiye azampatsa za kudya. Eliya ana cita zimene Mulungu anamuuza iye. Pamene anadza mumzinda muja, ana ona mkazi wamasiye, ndipo anati, "Ndipatse mkate. Ndipatse madzi." "Mkazi wamasiye uja anati ndili nazo zazing'ono zokwanila ine ndi mwana wanga cabe. Pemene tizadya izi tizafa pakuti ndi zimenezi cabe.



Kaisara Augusto analamulira dziko la Aroma. Anatumiza mau kuti onse anthu ayene.a kuwerengedwa. Kaisara Augusto anafuna ciwerengelo ca madzina a anthu kuti asonkhe misonkho. Aliyense apite kumudzi wace mwini. Conco Mariya ndi Yosefe anapita ku Betelehemu, ku mudzi wawo. Yesu, mpululumutsi anali kubwera mu dziko.

MAFUNSO

Werengani mau apa mtima coyamba.

1. Kodi ndinu osangalala?

2. Mumamvera lamulo la Mulungu?

3. Kodi mukalikufunabe mpulumutsi?

ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Yesaya 41:10-20 |
| Laciwiri | Yesaya 42:5-16 |
| Lacitatu | Yesaya 43:1-13 |
| Lacinai | Yesaya 44:1-8 |
| Lacisanu | Yesaya 45:1-13 |
| Loweruka | Yesaya 51:1-15 |
| Lasabata | Yesaya 52:1-15 |

Mulungu, ndipo anaphunzira zambiri pa lamuloli. Mulamulo la Mulungu, ana ona zimene zinali kondweletsa munthu. Werenga ndime izi ndi kuona ngati muzapeza, zimene zinakondweletsa munthu. Liu lakuti dala litanthauza kuti

Masalmo 119:1-8

*1 Odala angwiro m'mayendedwe ao, Akuyenda*
*m'cilamulo ca Yehova. 2 Odala iwo akusunga*
*mboni zace, Akumfuna ndi mtima wonse; 3 Inde,*
*sacita cosalungama; Ayenda m'njira zace. 4 Inu*
*munatilamulira, Tisamalire malangizo anu ndi*
*cangu. 5 Ha! mwenzi zitakhazikika njira zanga.*
*Kuti ndisamalire malemba anu. 6 Pamenepo sindi*
*dzacita manyazi, Pakupenyerera malamulo anu onse.*
*7 Ndidzakuyamikani ndi woongoka, Pakuphunzira*
*maweruzo anu olungama. 8 Ndidzasamalira male-*
*mba anu: Musandisiye ndithu.*

Kodi mwapeza cimene munthu asangalala naco? Mu ndime yoyamba imatiuza ife kuti munthu wosangalala amatsata lamulo la Mulungu. Ndime yaciwiri imatiuza ife kuti munthu wosangalala amamvera Mulungu. Munthu wosangalala amafuna Mulungu pa kupephera ndi kuwerenga Buku Lopatulika. Mu ndime ya cisanu itiuza ife kuti pamene munthu amamva kukhala wosangalala, amapepha kwa Mulungu ndi kunena kuti. Ha! Mwenzi zitakhazikika kuti ndisamalire malemba anu m'mene munditsogolera. Mundime ya cisanu ndi zitatu, olemba anena kuti, "Musandisiye ndithu ndizasamalira malemba anu."

## DZIKO NDILOKONZEKA NDI YESU

Luka 2:1-3

*1 Ndipo kunali masiku aja, kuti lamulo*
*linaturuka kwa Kaisara Augusto kuti dziko lonse*
*lokhalamo anthu lilembedwe; 2 ndiko kulembera*
*koyamba pakhala Kureniyo kazembe wa Suriya.*
*3 Ndipo onse anamuka kulembedwa, munthu ali*
*yense ku mudzi wace.*



Eliya anati ndipatse ine coyamba, ndiye pambuyo pace udye iwe ndi mwana wako. Mkazi iwe uzakhala ndi ufa ndi mafuta kufikila mvula itagwanso. Mkazi uja anacita monga Eliya ana muuza iye. Mkazi uja ndi mwana wace uja anakhala ndi cakudya monganso anakhala ndi Eliya.

## KUBWELELA KU ISRAYELI

Zaka zitatu zinapita kopanda mvula. Ndipo Mulungu ana uza Eliya ku bwelelanso ku Israyeli, ndi ku uza Ahabu kuti Mulungu azabweletsa mvula. Akavalo ndi a bulu amene anali a Ahabu anafuna mauzu ndi madzi. Ahabu ndi m'neneli obadiya anayamba kufuna madzi. Ahabu ana funanso Eliya. Tsopano Eliya anoona Obadiya ndipo anatuma mau kwa Ahabu kuti aku mane naye.

Ahabu anadza ku kumana ndi Eliya. Pamene Ahabu anoona Eliya anati, kodi ndiwe amene wa mvuta a Israyeli? Eliya anati iai, koma ndinu. Mwapita ku Baala osati Mulungu. Tsopano bweletsani anthu onse Israyeli ndi onse amene asata mafano ansembe ku phiri.

## KODI BAALA NDI MULUNGU

Ahabu ndi anthu a Israyeli anadza ku phiri, ndi ansembe amafano anadza ku phiri. Eliya anaima nati, mukayika-kayika kufikila liti? Ngati Yehova ndiye Mulungu msateni iye; ngati ndi Baala msateni iye. Ndipo Eliya anawauza ndipo Eliya anauza ansembe a Baala, phani ng'ombe ndi kuika pa guwa ndipo muyike pa guwa ndiye muitane inu dzina la Mulungu wanu Baala. Tsono ana itana pa dzina la Mulungu wa Baala kuti Mulunguyo ayankhe ndi moto. Anthu a Baala anacita zimene Eliya ana wa uza. Ana panga guwa ndipo anapha ng'ombe ndi kuika paguwa lija. Ndipo anayamba tsono ku itana dzina la Baala kuyambila m'mawa kufikila pa usana nati Baala timvele ife. Koma panalibe mau kapena wobvomeleza. Ndipo anakweza mau awo nadzitema ndi mipeni. Koma mulungu wa Baala sanalakhule ai.

## YEHOVA NDI MULUNGU

Eliya anamanga guwa ndipo anaika mwana wa ng'ombe pa guwalo. Ana thilanso madzipa nsembe ndi pa guwa. Eliya anafuna kuona kuti Mulungu ndani. Eliya na pephela kwa Mulungu. Anafunsa Mulungu kuti a waziwise anthu Mulungu woona. Pamene Eliya anapephela kwa Mulungu, pomwepo moto wa Yahova unagwa pa guwa la nsembe. Moto unagwa pa guwa ndi pa madzi amene anathilidwa pa nsembe ija. Anthu tsono anaona mphavu ya Mulungu. Anthu onse anagwa pa maso awo anati, "Yehova ndi Mulungu; Yehava ndi Mulungu."

MAFUNSO

1. Kodi muyesa kukhala pa kati pa maganizo awiri?

2. Mulungu wanu ndani?

3. Kodi mufuna kuyima pa nokha ndi kutumikila ambuye Mulungu?

ZOWELENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Ezekieli 36:26-38 |
| Laciwiri | Danieli 1:8-21 |
| Lacitatu | Danieli 3:13-28 |
| Lacinai | Danieli 6:10-23 |
| Lacisanu | Hoseya 6:1-11 |
| Loweluka | Yoweli 2:21-32 |
| Lasabata | Yohane 2:1-11 |



ndipo pambuyo pace Aaigupto anapam ana Aramu ndipo anapatanso Yerusalemu.

Moyowa a Yuda sunali woipa pamene anali muulamuliro wa Aaigupto. Anthu aci Aaigupto anawa citira zabwino a Yuda. Anali ndi a Yuda amene analemba Buku Lopatulika muci Helene. Anthu ambiri tsono anakhala akuwerenga mau a Mulungu ndikumva za pangano la mpulumutsi. Mulungu anali kukonze keradziko za kubwera kwa Yesu.

## ARAMU

Moyo wa a Yuda sunali wapafupi pa ulamuliro wa Aramu. Atsogoleri a Aramu anafuna kuti a Yuda nawonso apembedze a milungu aci Helene. Aramu anasewenzetsa kacisi wa Mulungu pa kupembeza milungu yao. Iyi siinali njira ya Mulungu. Ayuda anakwiya.

## AYUDA ANAMENYANA NAWONSO

Mu Yuda wansembe ndi ana ace ana tsogolera a Yuda kuka menyana nkhondo ndi Aramu. Anatenganso Yeresalemu kucoka m'manja mwa Aramu. Ana, awa nsembe uyu, ana lamulira Yerusalemu. Ana tsukakacisi. Anabweretsa ci pembezo coyenera ca Mulungu kwa Ayuda.

## AROMA

Aroma anayamba kutenga maiko amene azungulira Yerusalemu. Pambuyo pace, anatenganso mzinda wa a Yuda. Moyo wa a Yuda unali wobvuta pa ulamuliro wa Aroma. Aroma anali ndi atsogoleri olimba mtima amene ana funa kuti a Yuda akhale ndi msonkho waukuru. Komanso kucitika kwa izi zonse, Mulungu analikukonzekera dziko pa zakubwera kwa Yesu.

## LAMULO

Paulamuliro wa Aroma, a Yuda anayang'anira mpulumutsi. Ana phunzira lamulo la

MUTU 11

## PAKATI PACIPANGANO CAKALE NDI CA TSOPANO

PHUNZIRO LALIKURU LOCOKERA M'BUKU LOPATULIKA: Masalmo 1, 119:1-16 Luka 1:57 ndi 2:3.

MAU A MULUNGU A MPHUNZIRO LALERO: Masalmo 119:1-8, Luka 2:1-3.

MAU APA MTIMA: *"Ndinawabisa mau anu muntima mwanga kuti ndisalakwire inu."*
*Masalmo 119:11.*

Kodicinacitika kwa a Yuda ndi cotani pa nthawi ya cipangano ca kale ndi ca tsopano? Kodi anakhala na umoyo waubwino pamene anayembekeza Yesu, mpulumutsi, kubwera?

Buku lathu Lopatulika siliti fotokozera zimene zinacitika kwa a Yuda pa zaka izi. Tingathe ku yang'ana mu mabuku ambiri yakale kuona za miyoyo ya a Yuda.

Taphunzira kale m'mene Mulungu ana bwezera anthu aci Yuda kucoka ku Babulo kupita ku Yerusalemu. Anayamba kupembeza Mulungu. Mulungu analongezanso kuti azatumiza mpulumutsi.

### AHELENE

Coyamba a Helene anatenga Yerusalemu. Anatenganso maiko ena ambiri. Anthu amene anakhala m'maiko amenewa, anaphunzira ciyankhulidwe ca ci Helene. Mulungu anakhala akukonzera anthu cipangano catsopano.

### AAIGUPTO

Maiko otsogololedwa ndi a Helene anagawanikana. Aramu analamulira maiko ena, ndi Yerusalemu yomwe. Aaigupto ana lamulira maiko ena. Aaigupto ndi Aramu anamenya nkhondo zambiri;



MUTU 3.

## CIWELUZO CA MULUNGU PA ISRAYELI

PHUNZILO LALIKURU LA M'BUKU LOPATULIKA: Yesaya 4:1-5:14; Amosi 7-8, 2 Mafumu 17.

MAU AMULUNGU APHUNZILO LA LERO: 2 Mafumu 17: 9-18.

MAU APAMTIMA: *"Bwererani kuleka nchito zanu zoyipa, nimusunge malamulo anga ndi malemba anga, monga cilamulo conse ndinacilamulira makolo anu, ndi ku citumizira inu mwa dzanja la atumiki anga aneneri.*
*2 Mafumu 17:13.*

Mphunziro lathu lotsiliza, tava m'mene Eliya analongoza anthu kwa Mulungu. Mulungu anacita cozizwitsa ku anthu kuti aone. Mulungu anaonetsa anthu kuti iye ndi Mulungu. Anayankha pepherola Eliya. Anthu ana ona cozizwitsa cimene Mulungu ana cita. Koma anthu sana sinthe. Ana pitiliza kupembeza ma Baala. Mafumu anasitha. Koma Mafumu ambiri sana sate Mulungu. Israyeli sana pite kwa Mulungu. Tiyeni tione cimo la Israyeli.

2 Mafumu 17:9-12

*9 Ndipo ana a Israyeli ana cita m'tseri zinthu zosayenera pa Yahova Mulungu wao, nazimangira misanje m'midzi mwao monse ku nsanja ya olonda ndi ku mudzi walinga komwe, 10*
*Nadziimikira zoimititsa ndi zifanizo pa citunda ciri conse cacitali, ndi patsinde pa mtengo uli wonse wogudira, 11 nafukizapo zononkhira pa misanje yonse, monga vmo amacitira amitundu amene Yehova adawacotsa pamaso pao, nacita zoipa kuutsa mkwiyo wa Yehova, 12 natumikira mafano amene Yehova ana wanena nao. Musacita ici.*

Anthu a Israyeli anaganiza kuti aza bisa Mulungu zoipa zao. Anadziwa kuti Mulungu a wauza kuti sayenera kucita zinthuizi. "Koma anati tiza zibisa izi. Mulungu sazaziwa, izikuti tiri kuzicita ife."

Anthu ana manga malo opepheleramo m'mi-zinda yonse. Anthu amene anapembeza mafano anakhala mu Israyeli. Anthu Israyeli ana khala akupembezanso milungu ya Baala. Anthu a Israyeli ana panga mafano. Anapanga mafano a mitengo ndi miyala. Mafano ena anaoneka ngati anthu. Mafano ena anaoneka ngati nyama zamthengo. Mafano awa anapangidwa ndi anthu. Anthu anaika mafano awa pa citunda ciliconse cacitali. Anaziimikira pa mtengo wogudila uli onse. Zinthu izi zina kwiyisa Mulungu.

Zinthu izi zina kwiyisa Mulungu. Mulungu ana uza Israyeli kuti sayenera kupembeza mafa-no. Koma a Israyeli anacita zinthu izi ndipo Mulungu anawa kwiyila.

## KUSINTHANSO KWINA

Mulungu sazaweruza a Israyeli tsopanolino. Kapena anthu azavera Mulungu tsopano. Angasi-nthe mwina mwace. Werengani zimene anacita a Israyeli mu 2 Mafumu 17:13-17.

*13 Ndipo Yehova anacitira umboni Israyeli ndi Yuda kwa dzanja la m'neneri aliyense, ndi malaudi aliyense, ndi kuti, bwerani kuleka nchito zanu zoipa, nimusunge malamulo anga ndi malemba anga monga mwa cilamulo conse ndina cilamulira makolo anu, ndiku citumizira inu mwadzanja la a tumiki anga aneneri. 14 Koma sanamvera, naumisa khosi lao, monga khosi la makolo ao amene sana khulupilira Yehova Mulungu wao. 15 Ndipo anakaniza malemba ace, ndi cipangano anacicita ndi makolo ao, ndi mboni zace ana wacitira umboni nazo, natsata zopanda pace, nasanduka opanda pace, natsata amitundu owazinga, amene Yehova adawalamulira nao, kuti asacite monga iwowa. 16 Ndipo anasiya*



ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Yesaya 2:1-10 |
| Laciwiri | Yesaya 6:1-13 |
| Lacitatu | Yesaya 11:1-10 |
| Lacinai | Yesaya 26:1-9 |
| Lacisanu | Yesaya 32:1-8 |
| Loweruka | Yesaya 35:1-10 |
| Lasabata | Yesaya 40:1-11 |

Anthu sanamumvera mpulumutsi. Anthu anaganiza kuti anabvutika cifukwa ca cimo lace. Sanamvetse kuti ndi cimo lao lotani limene linabweza Yesu kubvutika. Yesu anabvutika ndi kutifela ife pa mtanda kutibweretsera ife mtendere. Mtendere uyu uli ndi Mulungu m'mitima mwathu.

M'neneri Yesaya ananena kuti mu ndime ya cisanu ndi imodzi kuti tonse tiri ngati nkhosa. Tifuna kupita m'njira za ife tokha. Nthawi zonse sitimalondola M'busa wathu. Tiyenera kubvutika cifukwa ca maonekedwe azinchito zathu zoipa. Koma Mulungu atumiza mpuluitsi kukhala m'busa wathu. Anapatsa mtima wace pa mtanda kuti tingapeze khola kapena thambo. Yesu anauka kwaakufa ndipo ali wamoyo lero. Anali nayo mphamvu ya kutikhululukira macimo athu ndi kutipatsa ife moyo wosatha.

Kodi mwa socela mucipululu lero? Yesu akupatsani inu njira yabwino ku thambo la kumwamba. Anapatsa moyo wace pamtanda kuti inu mukhale nawo moyo wasatha. Ndi ciani cimene muyenera kucita kuti mukhale ndi moyo wosatha? Muyenera kukhulupilira kuti Yesu akhoza kukupulumutsani inu kucokera ku macimo anu. Tsono muyenera kupepha kuti amukhululukire reni macimo anu ndi kuti akhale mpulumutsi wa moyo wanu.

MAFUNSO

1. Kodi anthu ankadziwa mpulumutsi wolonjezedwa?

2. Ndi cifukwa ninji mpulumutsi ankanabvutika?

3. Kodi inu mwacimwa?

4. Kodi mudziwa mpulumutsi, Yesu Kristu?



*malamulo onse a Yehova Mulungu wao, nadzipangira mafano oyenga, ana ang'ombe awiri, napanga cifanizo, nagwadila khamu lonse la kuthambo, natumikira Baala. 17 Napititsa ana ao amuna ndi akazi kumoto, na ombezaula, nacita za myanga, nazigulitsa kucita zoipa pamaso pa Yehova, kuutsa mkwiyowace.*

Mulungu anapatsa Israyeli mpata wina. Anatumiza a neneri ndi anthu anzeruku Israyeli. Mulungu anati kwa a Israyeli, "Cokani ku macimo anu. Sungani malamulo anga. Sungani malemba anga. Citani monga a neneri anga a nena."

Koma Israyeli sanamvera Mulungu sanamtha Mulungu. Ana umitsa mitima yao. Anacita ngati Mulungu sanali Mulungu. Anacita monga ngati Mulungu sanawauze. Anthu a Israyeli anatsata anzao. Anapembeza ma Baala ndi milungu yosinasiyana. Anthu ana pembeza moto. Analamulira ana kupita pa moto. Iyi inali njila yao ya kupembeza. Anthu anasewenzetsa ufiti. Anasewenzetsa masenga ndi nyanga, Mulungu anati, "Izi zonse ndizoipa." Osasewenzetsa izi. Anthu a Israyeli ana zigulitsa okha ku zoipa. Ngakhale lero, anthu ena amakhulupilira mu masenga koma osa khulupilira Mulungu.

## MULUNGU AWERUZA

2 Mafumu 17:18

*18 Cifukwa cace Yehova ana kwiya naye Israyeli kwakukuru, nawacotsa pamaso pace osatsala umodzi, koma pafuko la Yuda lokha.*

Mulungu ana uza anthu a Israyeli kuti atembenuke, koma sananvere ai. Mulungu anawapatsa mipata yambiri. Sanafune kumvera. Tsono Mulungu ana cotsa Isreyli pa paso ace. Anakhala otaika pakatipa anzao. Israyeli sunali ufulu ai.

## NANGA INU

Mu mamvera mlaliki. Mumamvera aphunzitsi.

Mumawerenga Buku Lopatulika. Muma phunzila zimene zimene Mulungu afuna ifekuti ticite. Kodi mupitili labe kucita zoipa? Kodi mumayesa ku bisa zinthu zoipa zimene mucita? Kodi mukhulupirila kuti Mulungu anga muthandizeni kusintha? Kodi mwafunsa Yesu kuti akhale mwainu, mumtima? Azamuthandizani kuti musinthe.

MAFUNSO

1. Kodi a Israyeli anali anzeru pa kusamvera Mulungu? Chifukwa?

2. Kodi Mulungu ana komeramtima anthu a Israyeli ndi cilungamo?

3. Kodi inu mwamvera Mulungu?

ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Yohane 4:1-15 |
| Laciwiri | Yohane 4:19-30 |
| Lacitatu | Yohane 4:31-42 |
| Lacinai | Yohane 6:5-14 |
| Lacisanu | Yohane 6:22-35 |
| Loweluka | Yohane 6:53-68 |
| Lasabata | Yohane 7:31-37 |



Mu Aroma 10:16, mtumwi Paulo alemba mau a Mulungu monga amenewa.

Werengani mu Yesaya 53:2 m'mene Yesaya ananenera za mpulumutsi m'mene azakulila. Lembani mau osawa mu malo awa, pakuti anadziwa iye monga __________ ndi monga __________ kucoka mu ________________.

Mpulumutsi sankanakhala wokongola. Muzu omera m'thaka youma ulibe maonekedwe abwino. Anthu ambiri sangathe kuona paizo. Mphulumutsi sankanafuna anthu kuyangana iye.

Cipangano catsopano sicifotokoza m'mene mpululumutsi Yesu Kristu anaonekera, Sitidziwa mtundu wa thupi lace. Sitidziwa mtundu wa maso ace kapena tidziwa za utali wace.

Mau a Mulungu atiuza kuti Yesu ankana muzonda anthu. Ankanabvutika cifukwa ca anthu ena. Sanka na muona iye ngati Mpulumutsi.

## YESU MONGA MULUNGU ANAMUONA IYE

Yesaya 53:4-6

*4 Zoonadi Iye ananyamula zowawa zathu, ndi kusenza zisoni zathu; koma ife tinamuyesa wokhomedwa, wokanthadwandi mulungu, ndi wabvutidwa. 5 Koma Iye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu, natundudzidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife taciritsidwa. 6 Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse.*

M'neneri anati aliyense anacimwa. Cifukwa ca cimo lathu, tiyenera kubvutika. Koma mpulumutsi, sazacimwa, conco sayenera kubvutika. Koma Yesu, mpulumutsi, ankanatenga cimo lathu mongangati ndi la iye. Adzabvutika cifukwa ca ife. Werengani Aroma 3:23, 6:23.

Mulungu anati ku anthu, "Mverani! Ndili naco catsopano cakunena. Ici ndi ca Mpulumutsi, mtumiki wanga. Adzakhala mtumiki, koma iye adza kwezedwa m'mwamba. Adzakhala wamkuru." (Ndime 13)

Mpulumutsi sazaoneka monga anthu ana mganizira. Adzabvutika, ndi mavuto amenewa adzaonetsa iye kukhala mosiyana. Sazaoneka ngati anthu ena. (Ndime 14)

Mpulumutsi adzadabwitsa mitundu ya mbiri. Mafumu adzakhala odabwa pakumuona iye. Adzaganiza, kuti uyu ndi Mpulumutsi koma sim mene anatiuzira kuti maonekedwe ace adzakhala conco. (Ndime 15)

## YESU MONGA ANTHU ANA MUONERA

Yesaya 53:1-3

*1 Ndani wamvera uthenga wathu? Ndi mkono wa Yehova wabvumbulukira yani? 2 Pakuti ameneyo adzaphuka pamaso pace ngati mtengo wanthete, ndi ngati muzu womera m'nthaka youma; Iye alibe maonekedwe, pena kukongola; ndipo pamene timuona palibe kukongola kuti timkhumbe. 3 Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu; munthu wazisoni, ndi wodziwa zowawa; ndipo ananyozedwa monga munthu wombisira anthu nkhope zao; ndipo ife sitinamlemekeza.*

Werengani ndime 1 kaciwirinso. Tsono werengani ndime izi kucokera m'buku la Yohane 12:37-38.

37 Koma angakhale adacita zizindikilo zambiri zotere pamaso pao, iwo sanakhaulupilira iye; 38 Kuti mau a Yesaya m'neneri akakwaniridwe amene anati: "Ambuye wakhulupirira ndani kulalikira wakhulupirira ndani kulalikira kwathu, ndipo mkono wa Ambuye wabvumbulutsidwa kwa yani?





## KUUNJIKANA KWA ANTHU A MULUNGU

PHUNZILO LA M'BUKU LOPATULIKA: 2 Mafumu 18:1-8, 2 Mafumu 22:23, Yeremiya 25:1-7.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: 2 Mafumu 18:1-6, 2 Mafumu 23:21-7.

MAU APAMTIMA: *"Woipa asiye njira yace, ndi munthu wosalungama, asiye maganizo ace, na bwela kwa Yehova, ndipo Yehova azamucitira cifundo, ndi kwa Mulungu wathu, pakuti iye adza khululukira kopasa.*
*Yesaya 55:7.*

Kuunjika ndi kumene kucitidwa pakukonza zoipa. Mphunziro latha taona m'mene a Israyeli ana zigulitsila iwo wokha ku zoipa kapena ku ucimo. Ana pitiliza kusamvera Mulungu. Mulungu ana cotsa a Israyeli pamaso pace.

Kodi anthu aci Yuda anaphunzira kucokela kwa Israyeli? Mafumua awiri anayesa kusintha Yuda. Ana yesa kubweza Yuda kwa Mulungu. Welengani m'mene anacitila.

## MFUMU HEZEKIYA

2 Mafumu 18:1-6.

*1 Ndipo kunali caka cacitatu ca Hoseya mwana wa Ela mfumu ya Israyeli, Hezekiya mwana wa Ahazi, mfumu ya Yuda analowa ufumu wace 2 Ndiye wa zaka makumi awiri ndi zisanu polowa ufumu wace, nakhala mfumu zaka makumi awiri mphambu zisanu ndi zinai m yerusalemu, ndi dzina la mace ndiye Abi mwana wa Zekariya. 3. Nacita iye zoongoka pamasopa Yehova, monga mwa zonse adazicita Davide khololace. 4 Ana cotsa misanje naphwanya zoimilitsa, iaikha*

*cimkuwa. 5 Anakhulupilira Yehova Mulungu*
*wa Israyeli, atafa iye panalibe wakunga iye*
*mwa mafumu onse a Yuda. Ngakhale mwa iwookha-*
*lapo asanabadwe iye. 6 Pakuti anaumirira*
*Yehova osapambuka pambuyo pace, koma anasunga*
*malamulo amene Yehova ada wa lamurila Mose.*

Mfumu Hezekiya anakhulupilira Mulungu. Anayesa kukhala monga Mulungu ananera. Hezekiya ana mphwanya pa malo pamene panali mapembezo amafano. Ana mphwanya mafano onse muzidunswa. Nthawi ina Mose ana panga njoka ya mkuwa. Onani Numeri 21:4-9.

Anthu anasunga njoka iyi ndipo anayika mukacisi. Anakhala aku pembeza njoka koma osati Mulungu. Hezekiya ana ononga njoka ija mu zidunswa. Hezekiya anamvera Mulungu.

Hezekiya anamvera Mulungu. Anayesa kubweza anthu kwa Mulungu. Anatenga zinthu zonse zimene anthu anali ku zipembeza. Koma anthu sanasinthe munjira zawo.

## KUPEZA BUKU LA MULUNGU

Mfumu Hezekiya anafa. Mafumu ena analamulira Yuda. Anthu anapitilira kupembeza mafano. Mubuku la Yosiya, amene anatsata Mulungu anafuna ku bweza anthu kwa Mulungu.

Yosiya anayamba kukonzanso kacisi ndi anchito. Anakhala ndi anchito ku sesa m'kacisi. Mafumu ena analola kacisi kukhala ndi dothi ndi kuonongeka.

Pamene wa nsembe ana sewenza mukacisi, anapeza buku. Anati, ndapeza buku la malamulo munyumba ya Mulungu. Wansembe ana peleka buku lija ku mfumu. Pamene Yosiya anamva mau a Mulungu a m'buku muja, sanakondwa, anadziwa kuti a Yuda sanamumvera Mulungu. Mulungu adzaweruza Yuda monganso a Israyeli.





## PANGANO LA AMBUYE YESU

PHUNZIRO LALIKURU LA M'BUKU LOPATULIKA: Yesaya 9:2-7, 11:1-10, 52:13 ndi 5:12, 61-1-3, Mika 5:2-4.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Yesaya 52:13-15 53:1-3 Yohane 12:37-38.

MAU APAMTIMA: *"Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa, kwa ife mwana wa mwamuna wa patsidwa ndipo ulamulilo udzakhala pa phewa lace, ndipo adzamucha dzina lace wodabwitsa, wa uphungu, Mulungu wamphamvu atate wosatha kalonga wa mtendere."*
*Yesaya 9:6.*

Kwa makhumi ambiri Mulungu anakhala ndi pangano kwa anthu kuti adzatumiza Mpulumutsi. Mau akuti Mpulumutsi anena kuti wopelekedwa. Aneneri ananena kuti, "Mulungu adzatumiza mpulumutsi." Monga Mulungu ananena kwa Aneneri, ananena zinthu zambiri pazakubwera kwa Mpulumutsi amene iye ankantumidza. Aneneri anauza zinthuzi ku anthu. Anakhala ali kudikhira kubwera kwa Ambuye Yesu mpulumutsi.

## MPULUMUTSI, MTUMIKI

Yesaya 52:13-15

*13 Taonani, Mtumiki wanga udzacita mwanze-*
*ru; adzakwezedwa ndi kutukulidwa pamwamba, na-*
*dzakhala pamwambamwamba. 14 Monga ambiri ana-*
*zizwa ndi iwe Israyeli, momwemo nkhope yace*
*yaipitsidwa ndithu, kupambana munthu ali yense,*
*ndi maonekedwe ace kupambana ana a anthu; 15*
*momwemonso Iye adzawazawaza mitundu yambiri;*
*mafumu adzamtsekera Iye pakamwa pao; pakuti*
*cimene sicinauzidwa kwa iwo adzacione, ndi ci-*
*mene iwo sanamva adzazindikira.*

Anthu anaima pa modzi ndipo anapembeza Mulungu. Ezara anapephera, ndi kuyamika Mulungu cifukwa ca cikondi cace. Anthu anazipelekanso kwa Mulungu. Ndipo ananenanso kuti lamulo la Mulungu ndi labwino ndipo ndi loona. Anadziwitsanso lamulo la Mulungu. Angakhale akupitilira ndi pangano lace kwa iwo.

MAFUNSO

1. Nanga a Yuda napindula bwanji mu kuwerenga kwa lamulo la Mulungu?

2. Kodi mufuna cithandizo pakumvera mau a Mulungu?

3. Kodi mau a Mulungu ndi osiidwa kwa inu?

ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Masalmo 119;105-112 |
| Laciwili | Masalmo 121 |
| Lacitatu | Masalmo 126 |
| Lacinai | Masalmo 138 |
| Lacisanu | Masalmo 145 |
| Loweruka | Masalmo 148 |
| Lasabata | Yesaya 1:10-20 |



## KUWERENGA BUKU LA MULUNGU

Mfumu Yosiya ana yitana anthu kukacisi. Yosiya anawa werengela malamulo a Mulungu kwa iwo. Yosiya anapanga pangano ndi Mulungu. Yosiya anasunga kacisi ndi zonse zimene zina sewenzetsedwa ndi mapembezo a Baala. Anatentha zinthu zonse zimene anapembedzela milungu ina. Yosiya anayesa kucotsa zinthu zopembeza m'maso a anthu. Anayesa kutsogolela anthu kupembeza Mulungu.

## YOSIYA ALAMULA

2 Mafumu 23:21-25

*21 Ndipo mfumu inalamulira anthu onse,*
*kuti, mcitireni Yehova Mulungu wanu Paskha,*
*monga mulembedwa m'buku ili la cipangano. 22*
*Zedi silinacitika paskha letere ciyambire ma*
*siku oweruza ana weruza Israyeli ngakhale*
*m'masiku a mafumu a Israyeli, kapena mafumu a*
*Yuda, 23 koma Paskha ili analicitira Yehova mu*
*Yerusalemu, Yosiya atakhala, mfumu zaka khumi*
*mphambuzisanu ndi zitatu. 24 Ndiponso, obwe-*
*bwela, ndi openda, ndi aterafi, ndi mafano,*
*ndi zonyansa zonse zidaoneka m'dziko la Yuda*
*ndi mu Yerusalemu. Yosiya anazicotsa kuti*
*alimbitse mau acilamulo olembedwa m'buku,*
*adacipeza Hilikiya wansembe m'nyumba ya Yehova.*
*25 Ndipo asanabadwe iye panalibe mfumu wolunga-*
*ma naye, imene inatembenukira kwa Yehova ndi*
*mtima wace wonse, ndi moyo wace wonse, ndi*
*mphamva yace yonse, monga mwa cilamulo conse*
*ca Mose, atafa iyeyu sana ukanso wina wolingana*
*naye.*

Mulungu analamulira anthu kusunga paskha caka cili conse. Paskha inathandiza iwo kukumbukila za Aigupto ndi Mose. Ici cina thandiza anthu ku kumbukila m'mene Mulungu anawa cotsera iwo mu Aigupto mu ukapolo.

Anthu sanakhale ndi Paskha kwa nthawi ya itali. Ambiri a iwo anayiwala Mulungu. Yosiya ana lamulira anthu. "Sungani Paskha monga

mulungu anamu uzani kuti mucite.

Yosiya anayangana kwa Mulungu ndi mtima wace wonse. Anayesa kumvera malamulo a Mulungu. Koma Yosiya sanathe kusitha m'mitima ya anthu.

## NANGA INU?

Kodi mumaganizira Mulungu nthawi yonse? Mu mamvera malamulo a Mulungu? Werenganinso mau apa mtima.

MAFUNSO

1. Kodi mafumu anakayesa anthu kupenza Mulungu?

2. Ndi ciani cimene cimacitika ku munthu ngati apembeza Mulungu?

3. Mupembeza ndani?

ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Yohane 8:12-19 |
| Laciwiri | Yohane 8:28-40 |
| Lacitatu | Yohane 9:1-9 |
| Lacinai | Yohane 9:24-38 |
| Lacisanu | Yohane 10:24-38 |
| Loweruka | Yohane 11:41-52 |
| Lasabata | Yohane 12:20-32 |

*mukamwe zozuna, nimumtumizire gawo lace iye amene sanamkonzeratu kanthu; cifukwa lero ndilo lopatulikira Ambuye wathu; ndipo musamacita cisoni; pakuti cimwemwe ca Yehova ndico mphamvu yanu. 11 Ndipo Alevi anatontholetsa anthu onse, ndi kuti, Khalani muli cete; pakuti lero ndi lopatulika; musamacita cisoni. 12 Napita anthu onse kudya ndi kumwa, ndi kumwa, ndi tutumiza magawo, ndi kusekerera kwakukuru; popeza anazindikira mau amene adawafotokozera.*

Ezara ndi Alevi anawerenga kucokera m'buku. Anawerenga bwino. Onse anamvera. Ndipo anawathandiza kuti amvere bwino zimene anawafotokozera. Ezara ndi Alevi ana wathandiza kutanthauza mau aja.

Anthu anamvera mau amene Ezara anawerenga. Anayamba kulira, cifukwa cakuti anazindikira kuti Mulungu anali ndi pangano nao; Koma Sanatsate pangano la Mulungu. Anadziwa kuti anacimwa kwa Mulungu ndipo sanali okondwa.

Ezara anati, "Lekani kulira, ili ndilo tsiku lacimwemwe. Idyani cakudya ndipo patsani iwo amene alibe ca kudya. Ili ndi tsiku lopatulika." Anthu anacita monga m'mene Ezara ananena. Anakhala ndi cikondwelelo cacikuru cifukwa anamvera mau a Mulungu. Tsono anamvera bwino mau a Mulungu.

## MSONKHANO UNAPITIRIRABE

Msonkhano unapitililabe kwa masiku ambiri. Tsiku lililonse Ezara ndi Alevi anawerenga kucokera m'buku lacilamulo ku anthu. Ndipo anawa tanthauzira mau ace pa mbuyo. Poyamba anthu anadya. Anali ndi cikondwelero cacikuru. Koma m'mene anamvera za lamulo ndimo m'mene anadziwa za macimo awo. Analeka kudya, anaika matope pa mitu yawo ndipo anamvara masaka. Anacita ici kuonetsa zolakwa zawo ndi cisoni. Anafuna kucoka ku macimo awo.

Nehemiya 8:1-3

*1 Ndipo anthu onse anasonkhana ngati*
*munthu mmodzi ku khwalala liri ku cipata ca*
*kumadzi, namuuza Ezara mlembi atenge buku la*
*cilamulo ca Mose, cimene Yehova adalamulira*
*Israyeli. 2 Ndipo Ezara wansembe anabwera*
*naco cilamulo pamaso pa msonkhano, ndiwo*
*amuna ndi akazi, ndi yense wakumva ndi kuzi-*
*ndikira tsiku loyamba la mwezi wacisanu ndi*
*ciwiri. 3 Nawerenga m'menemo pa khwalala*
*liri ku cipata ca kumadzi kuyambira mbanda*
*kuca kufikira msana, pamaso pa amuna ndi akazi,*
*ndi iwo okhoza kuzindikira; ndi anthu onse*
*anacherera khutu buku la cilamulo.*

Kunali msonkhano wa anthu mu m'seu cifukwa cakuti a Yuda anafuna kumvera lamulo la Mulungu. Aliyense amene ana mvera analiko kumeneko, amuna, akazi ndi ana. Onse anabwera pa modzi kumvera lamulo la Mulungu. Ezara anaimilira pa maso pa anthu. Anawerenga kucokera ku lamulo la Mose. Anawerenga kocokera m'mawa mpaka m'mazuro. Anthu anakhala ali kumvera.

## KUWERENGA BUKU

Ezara anaimilira pakati pa anthu ndipo anawerenga kucokera mu lamulo la Mose. Malo anamangidwa cifukwa ca cimeneci. Ena anaimilira ndi iye. Athandiza. Werengani ndime izi ndipo mpeze zimene zinayankhulidwa pa msonkhano.

Nehemiya 8:8-12

*8 Nawerenga iwo m'buku mcilamulo ca*
*Mulungumomveka, natanthauzira, nawazindikiritsa*
*cowerengedwaco. 9 Ndipo Nehemiya, ndiye kaze-*
*mbe, ndi Ezara wansembe mlembiyo, ndi Alevi*
*ophunzitsa anthu, ananena ndi anthu onse, Lero*
*ndilo lopatulikira Yehova mulungu wanu, musa-*
*macita maliro, musamalira misozi. Popeza*
*anthu onse analira misozi pakumva mau a cila-*
*mulo. 10 Nonena naonso, Mukani, mukadye zonona,*





## CIWERUZO CA MULUNGU PA A YUDA

PHUNZIRO LALIKURU LA M'MBUKU LOPATULIKA: Yeremiya 7:26-52.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LA LERO: Yeremiya 26:1-16, 52:12-16.

MAU APAMTIMA: *"Cifukwa cace tsopano konzani njira zanu ndi macitidwe anu, ndi kumvera mau a Yehova wanu, ndipo Yehova adzaleka coipa cimene ananenera inu.*
*Yeremiya 26:13.*

Muphunziro lathu lija, taphunzira za mafumu awiri aci Yuda. Awa anali mafumu abwino amene anayesa-yesa kutsogolera anthu kuti atsate Mulungu. Madzina amafumu awa anali, Hezekiya ndi Yosiya. Yosiya anali mfumu yotsiliza ya Yuda. Pamene anafa, Yohayakimu mwana wace, anakhala mfumu.

Yohayakimu sanali mfumu yabwino. Yohayakimu anabweletsanso zinthu zonse zonyansa zimene mfumu Yosiya anayesa kucotsa.

Mulungu anakondabe anthu aci Yuda. Mulungu anapitiliza kutumiza a neneli ku Yuda. Anafuna anthu kucoka ku zipembezoza mafano. Mulungu anafuna kuti anthu apembeze iye. Yeremiya anali m'modziwa aneneli amene Mulungu anatumiza Yeremiya ku kacisi.

Mulungu anati, nena ku anthu. Uza anthu zonse zimene ndi zanena.

## YEREMIYA ALANKHULA

Yeremiya 26:1-16.

*1 Poyamba kukhala mfumu Yehayakimu mwana*
*wace wa Yosiya, mfumu ya Yuda, panadza mau awa*

*acokela kwa Yehova, kuti, 2 Yehova atero: Ima m'bwalo la nyumba ya Yehova, ndi kunena kwa midzi yonse ya Yuda, imene imadza kudzagwadira m'nyumba ya Yehova, mau onse amene ndikuuza iwe kuti unene kwa iwo; usasiyepo mau amodzi. 3 Kapena adzamvera, nadzatembenuka, yense kusiya njira yace yoipa; kuti ndileke coipa, cimene ndinati ndiwacitire cifukwa ca kuipa kwa nchito zao. 4 Ndipo iwe uziti kwa iwo, Yehova atero: Ngati simudzandimvera Ine kuyenda m'cilamulo canga, cimene ndaciika pamaso panu, 5 kumvera mau a atumiki anga aneneri, amene nditumа kwa inu, pouka mamawa ndi kuwatuma iwo, koma simunamvera; 6 pamenepo ndidzayesa nyumba iyi ifanane ndi Silo, ndipo ndidzayesa mudzi uwu citemberero ca kwa mitundu yonse ya dziko lapansi. 7 Ndipo ansembe ndi aneneri ndi anthu onse anamva Yeremiya alinkunena mau awa m'nyumba ya Yehova. 8 Ndipo panali, pamene Yeremiya anatha kunena mau onse amene Yehova anamuuza iye kuti anene kwa anthu onse, ansembe ndi aneneri ndi anthu onse anamgwira iye, ndi kuti, Udzafa ndithu. 9 Bwanji mwanenera m'dzina la Yehova, kuti, Nyumba iyi idzafanana ndi Silo, mudzi uwu udzakhala bwinja lopanda wokhalamo? Ndipo anthu onse anamsonkhanira Yeremiya m'nyumba ya Yehova.*

*10 Ndipo pamene akuru a Yuda anamva zimenezi, anakwera kuturuka ku nyumba ya mfumu kunka ku nyumba ya Yehova; ndipo anakhala pa khomo la cipata catsopano ca nyumba ya Yehova. 11 Ndipo anasembe ndi aneneri ananena kwa akuru ndi kwa anthu onse, kuti, Munthu uyu ayenera kufa; pakuti wanenera mudzi uwu monga mwamva ndi makutu anu. 12 Pamenepo Yeremiya ananena kwa akuru onse ndi kwa anthu onse, kuti, Yehova ananditumа ine ndinenere nyumba iyi ndi mudzi uwu mau onse amene mwamva. 13 Cifukwa cace tsopano konzani njira zanu ndi macitidwe anu, ndi kumvera mau a Yehova Mulungu wanu; ndipo Yehova adzaleka coipa cimene ananenera inu. 14 Koma ine, taonani, ndiri m'manja anu; mundicitire ine monga mokomera ndi*





# LAMULO LA MULUNGU LITSIMIKIZIDWA

PHUNZIRO LALIKURU LA M'BUKU LOPATULIKA: Nehemiya 8 ndi 9.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Nehemiya 8:1-2, 8:8-12.

MAU APAMTIMA: " *Mundizindikiritsa, ndipo ndiza sunga malamulo anu ndizawa samalira ndi mtima wanga wonse.*
*Masalmo 119:34*

Kutsimikidza kunena kuti kuimilira pa cina cace. Cimenenanso kuti kunena zinthu zabwino kapena zoipa. Ngati titsimikidza cinthu timanenanso kuti cinthu ciri cabwino kapena coipa. Taimilira pa cinthu cimene tanena kuti ciri bwino.

Muphunziro iri, anthu a "Mulungu ananenanso kuti lamulo linali bwino ndipo loonadi."

## EZARA

Ezara anali wansembe ndipo anakhala mu Babulo. Anaphunzira ndipo analemba malamulo a Mose.

Anthu mu Yerusalemu anatha kumanga kacisi ndi zipupa ku thawi iyi anapembeza Mulungu. Pambuyo pace analeka kupephera kwao. Anasiyatso kuwerenga lamulo la Mulungu. Amuna ena anakwatira azimai amene sanakhulupilire Mulungu. Ngakhale atsogoleri a chalichi anacita zimenezi.

Ezara anamva zimenezi. Anapita kwa mfumu, ndipo anafunsa, "Kodi siningatengeko a Yuda ena ndi kupita ku Yerusalemu?" Mfumu inabvomeleza ndipo Ezara uja ndi a Yuda ena anapita ku Yerusalemu. Mu Yerusalemu, Ezara anabweletsa anthu onse pamodzi ku msonkhano. Werengani ndime izi ndi kuona cimene cinacitika pa msonkhano uja.

## ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Msalmo 104:24-35 |
| Laciwili | Masalmo 107:1-9 |
| Lacitatu | Masalmo 107:21-31 |
| Lacinai | Masalmo 111:1-10 |
| Lacisanu | Masalmo 116:1-15 |
| Loweluka | Masalmo 118:1-14 |
| Lasabata | Masalmo 119:97-104 |



*moyenera m'maso anu. 15 Koma mudziwe ndithu*
*kuti, ngati mudzandipha ine, mudzadzitengera*
*nokha mwazi wosacimwa, ndi pa mudzi uwu, ndi*
*pa okhalamo ace; pakuti mwa ntheradi Yehova*
*wandituma kwa inu kuti ndinene mau onse awa*
*m'makutu anu. 16 Pamenepo akuru ndi anthu*
*onse anati kwa ansembe ndi kwa aneneri, Munthu*
*uyu sayenera kufa: pakuti watinenera ife*
*m'dzina la Yehova Mulungu wathu.*

Pamene munawerenga ndime izi munapeza cifukwa ninji Mulungu anatuma Yeremiya ku kamba ku anthu? Munapeza ciani mundime ya citatu? Kodi muna peza kuti Mulungu anapelekanso ku anthu mpata wina? Mulungu sanafune kuti awononge anthu. Anafuna kuti acoke ku macimo awo. Ngati anthu adzacoka ku ucimo kulangidwa sikungabwere kwa iwo. Mulungu adza khulululukira ngati adzabwera kwa iye.

M'malo mwa kupembeza Mulungu anapembeza kacisi. Sanakhulupilire mwa Mulungu. Mulungu anati ku anthu ngati simudzamvera aneneri anga, ndidza ononga kacisi uyu. Kacisi idzakhala ngati silo. Jerusalemu idza onongekanso.

Pamene kacisi isanamangidwe, silo anali malo amapephero. Anali malo m'mene malamulo Mulungu anasungidwa.

M'moyo wa Yeremiya, silo sunali mzinda. Anthu anaiwala malo amapephero. Anadza kuza pembedza kacisi mu Jerusalemu. Mulungu anauza anthu, Jerusalemu ndi kacisi zingakhale silo. Zinga iwalike.

### ANTHU

Kodi anthu anacitaciani? Anakana mau a Yeremiya. Sanafunekumvera. Anauza Yeremiya kuti adzafa cifukwa ca mau aja. Akuru-akuru anati, Yeremiva anaya nkhula zoipa pa Yerusalemu. Anati, ayenera kufa.

Yeremiya anati, "Ndikamba mau a Mulungu. Afuna inu kuti mu tembenuke ku njira zanu zoipa. Ngati mudzandipha mudzapha munthu

amene sanacite coipa."

Pamenepo ena akuru-akuru anati, munthu uyu sayenera kufa. Amayankhura za mau a Mulungu. Akuru-akuru aja anakumbukira mfumu Hezekiya. M'neneri anati Yerusalemu idza onongeka. Mfumu inabwerera kwa Yehova. ana muleka Yeremiya kuti akhale wa moyo.

## CIWERUZO

Yeremiya 52:12-15

*12 Mwezi wacisanu tsiku lakhumi la mwezi, ndico caka cakhumi ndi cisanu ndi cinai ca Nebukadirezara, mfumu ya ku Babulo, analowa m'Yerusalemu Nebuzaradani kapitao wa alonda, amene anaimirira pamaso pa mfumu ya ku Babulo: 13 ndipo anatentha nyumba ya Yehova ndi nyumba ya mfumu, ndi nyumba zonse za m'Yerusalemu, ngakhale zinyumba zazikuru zonse, anazitentha ndi moto. 14 Ndipo nkhondo yonse ya Akasidi, imene inali ndi kapitao wa alonda, inagumula makoma onse a Yerusalemu pomzungulira pace. 15 Ndipo Nebuzarandani kapitao wa alonda anatenga ndende anthu aumphawi, ndi anthu otsala amene anatsala m'mudzi, ndi amene anapandukira, kutsata mfumu ya ku Babulo, ndi otsala a unyinjiwo.*

Anthu amu Yuda anakana ku mvera Mulungu. Anapitilila mu zoipa zao. Babulo inali dziko la mphamvu. Babulo anagonjetsa Aigupto munkhundo. A Babulo aja anafuna kutenga Yuda. Anthu aci Yuda sanafoke. Maiko awiriwa anamenyana nkhondo kwa, kupambana caka cimodzi. Babulo inagonjetsa a Yuda. Anthu aku Babulo anatentha kacisi, nyumba ya mfumu ndi manyumba ena. Asirikali aku Babulo anaononga zinyumba za m'Yerusalemu. Anthu ambiri aci Yuda anatengedwa ku Babulo. Dziko la Yuda lina tengedwa muukapolo. Ciweruzo ca Mulungu cafika ku Yuda.

MAFUNSO

1. Kodi Mulungu anali okoma kwa a Yuda?



*lina logwira nchito, ndi lina logwira cida; 18 ndi omanga linga ali yense anamangira lupanga lace m'cuuno mwace, nagwira nchito motero. Ndipo woomba lipenga anali ndi ine. 19 Ndipo ndinati kwa aufulu, ndi olamulira, ndi anthu otsala, Nchito ndiyo yocuruka ndi yacitando, ndi ife tiri palace palace palingapo, yense atalikizana ndi mnzace; 20 pali ponse mukumva mau a lipenga, musonkhanire komweko kwa ife; Mulungu wathu adzatigwirira nkhondo.*

Anthu onse anchito anali okonzeka kumenyana ndi adani. Munthu aliyense anagwira nchito ndi dzanja limodzi ndipo dzanja lina anagwira lupanga. Munthu wina m'modzi anali ndi lipenga ndipo anaimilira pafupi ndi Nehemiya. Anthu omanga aja ana gwira nchito kufika palali pa cipupa. Nehemiya anati, "Mukamva mau a lipenga, musonkhane pa modzi. Mulungu azatigwirira nkhondo."

## CIKHULUPILIRO CI PAMBANA

Nehemiya 6:15-16

*15 Ndipo linga linatsirizika pa tsiku la makumi awiri ndi lacisanu la mwezi wa Eluli, titalimanga masiku makumi asanu mphambu awiri. 16 Ndipo kunali atacimva adani athu onse, amitundu onse akutizinga anaopa, nagwadi nkhope; popeza anazindikira kuti nchitoyi inacitika ndi Mulungu wathu.*

Masiku makumi asanu ndi mphambu ziwiri, anthu anamanga cipupa. Nehemiya ndi anthu anakhulupilira Mulungu. Sanasiye cifukwa ca mabvuto. Anatsiliza nchito. Adani awo sanamve bwino. Anakhala ndi mantha. Anadziwa kuti Mulungu anathandidza a Yuda.

MAFUNSO

1. Kodi Mulungu angagwiritse nchito anthu amene sadziwa iye?
2. Ndinjira yotani imene ili yabwino yocokeramo m'zobuta?
3. Kodi Mulungu ali nayo nchito ya padela ya inu?

Zaka zinapita. Mfumu Koresi anafa. Mfumu ina inali mu Babulo. Anapeza mau olembedwa ndi mfumu Koresi. Awa anali mau akuuza anthu aci Yuda kuti amange kacisi. Anatumiza zomangira ndi anthu enanso ku Yerusalemu. Mwamsanga anthu anasiliza kumanga kacisi.

Komanso Yerusalemu analibe zipupa kapena ma congo. Anthu anatsiliza nchito yomanga zipupa.

NEHEMIYA

Nehemiya anakhala mu Babulo. Anasewenzera mfumu. Mfumu ina mkhulupilira Nehemiya. Nehemiya anamva zazipupa za Yerusalemu. Anadziwa kuti nchito sinathe ai. Mfumu inatumiza Nehemiya ndi anthu ena ku Yerusalemu. Anapita kuti akathandize ku manga zipupa.

Nehemiya anapeza mavuto ambiri. Analiko adani anafuna kubvuta a Yuda. Anati, "Zipupa ndi zofoka. Ngakhale nkhandwe siingayende pa zipupa." Koma Nehemiya anapephera ndipo anthu anapitilira kusewenza. Adani aja anabweretsa asirikali. Anapangana kuti amenyane nao nkhondo a Yuda mu Jerusalemu. Nehemiya anapephera. Anapatsa anchito ace mikondo ndi malupanga. Anapitilizabe kusewenza.

CIKHULUPIRILO CA NEHEMIYA

Werengani ndime izi. Onaninso cina cimene Nehemiya anabwezera adani aja.

Nehemiya 4:15-20

*15 Ndipo kunali, pakumva adani athu kuti cinadziwika nafe, ndi kuti Mulungu adapititsa pacabe uphungu wao, tinabwera tonse kumka kulinga, yense ku nchito yace. 16 Ndipo kuyambira pamenepo gawo lina la anyamata anga anagwira nchito, ndi gawo Ina linagwira nthungo, zikopa, ndi mauta, ndi maraya acitsulo; ndi akuru anali m'mbuyo mwa nyumba yonse ya Yuda. 17 Iwo omanga linga, ndi iwo osenza katundu, posenza, anacita ali yense ndi dzanja lace*



2. Kodi Mulungu amalankhula ku anthu masiku ano? Motani?

3. Kodi Mulungu akali ku weruza anthu amene iwo akana kutembenuka ku macimo awo?

4. Kodi Mulungu alankhula kwa inu?

ZOWERENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Yohane 13:31-38 |
| Laciwiri | Yohane 14:1-14 |
| Lacitatu | Yohane 14:15-24 |
| Lacinai | Yohane 15:12-27 |
| Lacisanu | Yohane 16:1-16 |
| Loweluka | Yohane 17:1-15 |
| Lasabata | Yohane 18:1-14 |

MUTU 6

## CIKHULUPILIRO CA MULUNGU COSIIDWA

PHUNZIRO LALIKURU LA M'BUKU LOPATULIKA: Maliro 3:19-40, Ezekieli 18.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Maliro 3:19-33.

MAU APAMTIMA: *"Cifukwa cakusathedwa ife ndico cifundo ca Yehova, pakuti cisoni cacesicileka, cioneka catsopano m'mawa ndi m'mawa; mukhulupirika ndithu.*
*Maliro 3:22-23.*

## ANTHU ACISONI

Anthu ambiri aci Yuda anakhala m'malo acilendo. Anasiya kupembeza Mulungu. Anali anthu atsopano mu ukapolo kwa mfumu ya cilendo.

Ici cinabweretsa cisoni ku anthu aci Yuda kopambana. Anaganiza kuti kunalibe njila ya kuthawira. Anthu ena anati, ndicifukwa ninji tiyenera kuyesa? Mulungu ali wokalipa ndi ife. Atiiwara ife. Mulungu satimvera ife konse.

## NJIRA YA KUCOKERAMO

Yeremiya, m'neneri wa Mulungu anali wa cisoni nayenso. Yeremiya analinso m'tundu wa ciYuda. Anaona anthu ace ali ku vutika. Yeremiya ana ona m'mene anthu anali ndi cisoni. Koma Yeremiya sanakhale wa cisoni mopitilira. Ciyembekezo cinadza kwa Yeremiya ndi ku anthu ena. Ndime izi zizatifotokozera zimene zinacitika.

Maliro 3:19-33

*19 Kumbukirani msauko wanga ndi kusocera*
*kwanga, ndizo civumulo ndi ndulu. 20 Moyo*
*wanga uzikumbukirabe nuwerama mwa ine. 21*
*Ndili naco ciyembekezo popeza ndilingalira ici*



*nawalembenso, ndi kuti, 2 Atero Koresi*
*mfumu ya ku Perisiya, Yehova Mulungu Wam'mwamba anandipatsa maufumu onse a pa dziko lapansi, nandilangiza ndimmangire nyumba m'Yerusalemu, ndiwo m'Yuda. 3 Ali yense mwa inu a*
*anthu ace onse, Mulungu wace akhale naye, akwere kumka ku Yerusalemu, ndiwo m'Yuda, nakaimange nyumba ya Yehova Mulungu wa Israyeli; Iye ndiye Mulungu wokhala m'Yerusalemu. 4*
*ndipo ali yense wotsala pamalo pali ponse agonerapo iye, anthu a kumalo kwace amthandize ndi siliva, ndi golidi, ndi zoweta, ndi cuma, pamodzi ndi nsembe yaufulu ya kwa nyumba ya Mulungu iri ku Yerusalemu.*

Mfumu Koresi anatenga Babulo. Kodi anacita zinthu zimene a Yuda anaopa? Pamene a Yuda anatengedwa ku Babulo M'neneri Yeremiya anati, "Tsiku lina mudzabwera ku Yerusalemu." Tsiku tsono linadza lakubwerera. Mulungu anatumiza mfumu monga pa zakubwera.

Mfumu Koresi sanapembeze Mulungu. Koma Mulungu anagwedeza mtima wa Koresi. Mfumu inacita zonse zimene Mulungu anaika mu mtima wace. Werengani ndime ya ciwiri ndi kuti mpeze zimene Mulungu anaika mu mtima wa mfumu Koresi.

Ndani anakamanga kacisi? Werengani ndime ya citatu. Mfumu Koresi anati aliyense wobwerera ku Yerusalemu. M'yuda aliyense anathandiza kumanga kacisi.

Sionse a Yuda anabwerera ku Yerusalemu. Ena anakonda Babulo ndipo anakhala kumeneko. A Yuda amene anakhala ku Babulo anapeleka siliva ndi golidi kwa amene anapita ku Yerusalemu. Mfumu Koresi anabweza siliva ndi golidi ku Yerusalemu. Anthu anamanga guwa la nsembe ndipo anayamba kupembeza Mulungu. Koma ana cedwa ku manga kacisi.

Anthu anakhala aku manga ma nyumba. Anakhala akulima mbeu. Nthawi ina anakhala akucita zinthu zina. Panalibe nthawi imene inatsala ya kugwira nchito ku kacisi.

MUTU 8

## COSIIDWA CA MULUNGU CIMANGIDWANSO

PHUNZIRO LALIKURU LA M'BUKU LOPATULIKA: Ezara 1;6; Nehemiya 2:11-20, 4, 6:15-16

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Ezara 1:1-4, Nehemiya 4:15-20, Nehemiya 6:15-16.

MAU APAMTIMA: *"Koma tinamanga lingali ndi linga lonse linalumikizana kufikira pakati mpakati popeza mitima ya anthu inalunjika ku nchito." Nehemiya 4:6.*

Kodi nyumba yanu inaonongeka ndi moto kapena madzi? Mudziwa kubvuta kwace pakuma nganso nyumba ija. Anthu aci Yuda anakhala nganso nyumba ija. Anthu aci Yuda anakhala ndi zothetsa nzeru pa kumanganso Yerusalemu. Phunziro ili lizakufotokozerani zobvutazao.

Phunziro latha tinaphunzira kuti pamene anthu aci Yuda anali ku Babulo anakhala amantha. Anaopa kuti mfumu yatsopano idzatenga Babulo. Anaopa zimene mfumu iyi ika nacita kwa iwo. Zambiri zobvuta zinaimilira pakati paopa ku bwerera ku Yerusalemu. Mulungu analonjeza kuti adzawapatsa njira.

## MFUMU KORESI

Korsi mfumu ya Perisiya inali mfumu imene a Yuda anaopa. Ndime izi zizatiuza zimene Koresi anacita kwa a Yuda (Nzina lina la anthu aci Yuda).

Ezara 1:1-4

*1 Caka coyamba tsono ca Korsi mfumu ya ku Persiya, kuti akwaniridwe mau a Yehova m'kamwa mwa Yeremiya, Yehova anautsa mzimu wa Koresi, kuti abukitse amu m'ufumu wace wonse,*



*ndiyembekeza kanthu. 22 Cifukwa cakusathedwa ife ndico cifundo ca Yehova, pakuti cisoni cace sicileka. 23 Cioneka catsopano m'mawa ndi m'mawa; mukhulupilika ndithu. 24 Moyo wanga uti, gawo langa ndiye Yehova, cifukwa cace ndidzakhulupirira. 25 Yehova akhalira wabwino omlindira, ndi moyo womfunafuna. 26 Nkokoma kuti munthu ayembekeze ndi kulindirira modekha cipulumutso ca Yehova. 27 Nkokoma kuti munthu asenze gori ali wamng'ono. 28 Akhale payekha natonthole, pakuti Mulungu wamsenzetsa ciri-ilo. 29 Aike kamwa lace m'pfumbi, kapena ciripo ciyembekezo. 30 Atembenuzire wampanda tsaya lace, adzazidwe ndi citonzo. 31 Pakuti Yehova sadza taya kufikira nthawi zonse, 32 Anga khale alilitsa, koma adzacitira cisoni monga mwa kucuruka kwa zifundo zace. 33 Pakuti samasautsa dala, ngakhale kumvetsa ana a anthu cisoni.*

## MAPHUNZIRO ENA

Yeremiya anakumbukira Mulungu. Ndipo anapephera. M'mene Yeremiya anapephera, anaphunzira zinthu zina zimene zinampatsa ciyembekezo. Werenganinso mu ndime 25 ndi 27. Lembani mau ofunika mu mizere. "Mulungu aliwabwino kwa iwo aku ______________________ kamba kaiye, ku mtima umene ______________________ iye." Citanthauza ciani pa kunena kuti, kuyembekeza Mulungu? Ngati mubvutika, kodi mumakhala pansi wa cisoni? Ayi! Munthu ayembekeza Mulungu. Amadziwa bwino za masiku akutsogolo.

Ndime ya 27, "Nkokoma kuti munthu asenze golilace," cimatanthauza kuti kuphunzitsa munthu pamene ali wa m'ng'ono. Tingaphunzire zinthu zambiri kucokera ku makolo kapena azi-phunzitsi anthu. Tingaphunzirenso kucokera m'zowawa ndi m'kubvutika. Ngati tizaphunzira m'zinthu izi, tikodza kuphunzira kukhala ndi ciyembekezo mwa Mulungu.

Yeremiya anaphuzira kuti Mulungu safuna kuti anthu azibvutika. Anthu ena amazibwelesera mabvuto mwa iwo okha. Sayembe keza pa

Mulungu. Ngati mabvuto abwera, Mulungu sazalekelera kuti mabvuto apitilire. Yeremiya anafuna anthu kuti akhale ndi ciyembekezo ca tsopano. Ana lemba zonse zimene iye anaphunzira. Ici cinapatsa ciyembekezo ku anthu ena. Anthu ena anatembenukira kwa Mulungu. Anayembekeza pa Mulungu.

## EZEKIELI

Ezekieli analinso m'neneri wa Mulungu. Anakhala ndi anthu ena a Israyeli. Anthu awa a Israyeli, anakhala ku malo acilendo.

Mulungu anaitana Ezekieli kuti akambe za ciyembekezo ku anthu amene anali akapolo. Anthu anali kunena, "Tibadala mwa makolo anthu, ucimo. Mulungu sali wa cifundo kwaife." Anali okonzeka kusiya. Izi ndizimene Ezekieli anawafotokozera.

Ezekieli 18:30-32

*30 Cifukwa cace ndidzakuweruzani inu,*
*nyumba ya Israyeli, yense monga mwa njira zace,*
*ati Ambuye Yehova. Bwerarani, nimutembenukire*
*kuleka zolakwa zanu zonse, ndipo simudzakhumu-*
*dwa nazo, ndi kuonongeka nayo mphulupulu. 31*
*Tayani, ndi kudzicotsera zolakwa zanu zonse*
*zimene munalakwa nazo, ndi kudzifunira mtima*
*watsopano, ndi mzimu watsopano; pakuti mudza-*
*feranji inu, nyumba ya Israyeli? 32 Pakuti*
*sindikondwera nayo imfa ya wakufayo, ati Ambu-*
*ye Yehova; cifukwa cace bwererani, nimukhale ndi*
*ndi moyo.*

**Ezekieli anati, "Palibe munthu ali wocimwa cifukwa ca cimo la wina. Munthu aliyense ama yankha Mulungu ndi zimene acita. Muyenera kuyamkha mwa inu nokha." Ezekieli anauza anthu kuti Mulungu safuna munthu aliyense kuti afe cifukwa ca cimo lace. Mulungu afuna kuti munthu aliyense acoke m'macimo ace. Mulungu afuna aliyense kubwera kwa iye ndi kukhala wa moyo.**



Mulungu anawa khululukira a Yuda zolakwa zao. Anapangana nawo kuti adza wabwedza ku dziko lawo. Anakhala aku ona ulemelero wa Mulungu.

M'neneri Yesaya anati, "Mulungu akupatsani mau ace. Pitani. Nenani nkhani ya bwino ku anthu onse. Auzeni kuti, onani Mulungu ali ndi inu kwa nthawi zonse. Akukondani. Akukhululukirani. Akhala wamuyayaya.

MAFUNSO

1. Kodi Mulungu ayiwara dziko lathu? Kodi Mulungu akuyiwalani inu?

2. Kodi njira ya kubwereranso ku Yerusalemu inali yobvuta? Kapena inaoneka yobvuta?

3. Kodi Mulungu amathandiza anthu ace motani masiku ano?

ZOWELENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | 1 Akorinto 15:47-58 |
| Laciwiri | 1 Akorinto 16:1-14 |
| Lacitatu | 2 Akorinto 5:11-21 |
| Lacinai | 2 Akorinto 6:1-10 |
| Lacisanu | 2 Akorinto 8:1-12 |
| Loweluka | 2 Akorinto 11:16-30 |
| Lasabata | Masalmo 103:1-11 |

Mundime ya cisanu Mulungu awauza kuti iye anali nao. Anakhala auona ulemelero wa Mulungu. Ndiponso anakhalanso akuona kuti Mulungu anali nao.

## DZIKO LA AMBUYE MULUNGU WATHU

Yesaya 40:6-8

*6 Mau a wina ati, Pfuula. Ndipo ndinati,*
*Kodi ndipuule ciani? Anthu onse ndi udzu,*
*ndi kukoma kwao konse kunga duwa la m'thengo;*
*7 udzu unyala, duwa lifota; cifukwa mpweya wa*
*Yehova waombapo; zoonandi anthu ndi udzu. 8*
*Udzu unyala, duwa lifota, koma mau a Mulungu*
*wathu adzakhala nthawizacikhalire.*

Mulungu anauza m'neneri anati munthu ali anthu. Anafuna kuti anthu amvere. M'neneri anati munthu ali monga ngati udzu, zinthu zimene acita zili ngati duwa. Zinthu izi zingakhale zazikulu ndi zokoma. Ndiponso zikhoza kufa ndi mphepo yaikuru yotentha. Munthu ndi zimene acita zingafote. Ngakhale mitundu ya anthu ingafe m'njira imene iyi. Koma mau a Mulungu anakhalacikhalire. Palibe mphamvu imene ingacotse mau a Mulungu.

## UMISONI WA A YUDA

Yesaya 40:9-11

*9 Iwe amene utengera mau abwino ku Ziyoni,*
*kwera iwe pamwamba pa phiri lalitari; iwe*
*amene utengera mau abwino ku Yerusalemu, kweza*
*mau ako ndi mphamvu, kwezetsa usaope, nena ku*
*midzi ya Yuda, Taonani, Mulungu wanu! 10 Taona-*
*ni, Ambuye Yehova adzadza ngati wamphamvu,*
*ndipo mkono wace udzalamulira; taonani, mphoto*
*yace iri ndi Iye, ndipo cobwezera cace ciri*
*patsogolo pa Iye. 11 Ilye adzadyetsa zoweta*
*zace ngati mbusa, nadzasonkhanitsa ana a*
*nkhosa pa capa pace, nadzawatengera pa cifuwa*
*cace, ndipo adzatsogolera bwino bwino zimene*
*ziyamwitsa.*

MAFUNSO

1. Mumacita ciani ngati cisoni ndi mabvuto abwera pa inu?
2. Kodi mumakumbukira cikondi ca Mulungu kwa inu?
3. Kodi mumayamika mulungu pa madalitso ace kwa inu?
4. Kodi mumapedza ciyembekezo catsopano mwa Mulungu?
5. Ndizotani zimene mulinazo za kuyamika Mulungu?

ZOWELENGA TSIKU NDI TSIKU

| | |
|---|---|
| Lolemba | Yohane 18:28-40 |
| Laciwili | Yohane 19:1-11 |
| Lacitatu | Yohane 19:13-22 |
| Lacinai | Yohane 19:28-42 |
| Lacisanu | Yohane 20:19-31 |
| Lowekuka | Yohane 21:9-17 |
| Lasabata | 1 Akorinto 15:20-28 |

## PANGANO LA KUBWERELANSO

PHUNZIRO LA M'BUKU LOPATULIKA: Masalmo 126, 137:1-6, Yesaya 40:44, 51:1-16, Yeremiya 31.

MAU A MULUNGU APHUNZIRO LALERO: Yesaya 40:1-11.

MAU APAMTIMA: *"Ndipo oomboledwa a Yehova adzabwera nadzafika ku Ziyoni; ndi nyimbo ndi kukondwa kosatha kudzakhala pa mitu yao; adzakhala m'kusangalala ndi kukondwa, ndipo cisoni ndi kuusa moyo kudzacoka."*
*Yesaya 51:11.*

Anthu aci Yuda anakhala kubabulo kwa zaka makhumi asanu. Anthu ena a iwo anabadwila ku zonse za umoyo wao.

Anthu awa aci Yuda nthawi zambiri anakhala akufunsa, "Kodi Mulungu ayiwara anthu ace?" Adziwa kuti anali m'malo atsopano aku Babulo cifukwa ca macimo awo. Anafunsa "Kodi tizalipila kwa nthawi yotani ku zamacimo athu? Kodi ana athu aza bvutika cifukwa ca macimo athu?"

Cinthu cina cinacitika cimene cinadetsa nkhawa a Yuda kopambana. Dziko la Babulo likanagwa. Mfumu ina inakhala ikucita nkhondo ndi anthu a mu Babulo. Ndi ciani cikanacitika kwa a Yuda ngati mfumu ija inalanda Babulo? Anthu aci Yuda anada nkhawa.

## MULUNGU ANALANKHURA

Mulungu anapatsa mau kwa m'neneri kuti auze anthu. Mau ace ndi awa.

Yesaya 40:1-2

*1 Mutonthoze mutonthoze mtima wa anthu*



*ati Mulungu wanu. 2 Munene inu zotonthoza mtima kwa Yesusalemu numuofuulire kwa iye, kuti nkhondo yace yatha, kuti kuipa kwace kwakhululukidwa; kuti iye walandira mowirikiza m'dzanja la Yehova, cifukwa ca macimo ace onse.*

Mulungu anayankhula mwa cifundo ndiponso mwa ubwino ku anthu acisoni. Anthu ace anali akuda nkhawa tsono anafuna kuti awaonetse cikondi cace.

Mu ndime ya ciwiri Mulungu awafotokozera anthu kuti ucimo wao wakhululukidwa. Anati, "Mwalipira cifukwa ca macimo anu, tsono mwa masulidwa."

## NJIRA YA YEHOVA

Yesaya 40:3-5

*1 Mau a wopfuula m'cipululu, Konzani njira ya Yehova, lungamitsani m'dziko loti se khwalala la Mulungu wathu. 4 Cigwa ciri conse cidzadzazidwa, ndipo phiri liri lonse ndi citunda ciri conse zidzacepetsedwa, ndipo zokhota zidzaongoledwa, ndipo zamakolokoto zidzasalala; 5 ndipo ulemerero wa Yehova udzabvumbulutsidwa, ndipo anthu onse adzauona pamodzi, pakuti pakamwa pa Yehova panena comweco.*

Kodi anthu aci Yuda akanapitanso ku Yerusalemu? Kunali maloo obvuta pakati pa Babulo ndi Yerusalemu. Anaganiza kuti saza pitanso ku Yerusalemu. Kunali thengo laikulu pakati pa Babulo ndi Yerusalemu. M'zinda wa Yerusalemu unatenthedwa. Ngakhale kacisi yao inaonongeka. Unga khale m'tundu wobwanji umene uli womasulidwa?

Mulungu analankhula ku anthu kudzera kwa Yesaya m'neneri. Anati "Ndidziwa kuti njira iyi ndi yobvuta koma ndifuna - funa njira yaiwe." Mulungu anauza anthu kukonzeka. Anaona Mulungu panchito. Anthu anaganiza kuti Mulungu sanali ndi iwo chifukwa kacisi ana onongeka.